Khalani ndi Makhalidwe Amene Mulungu Amasangalala Nawo (Gawo 2)

Nkhaniyi yachokera m’mutu 12 wa buku lakuti, *Zimene Baibulo Limaphunzitsa* lomwe likupezeka pa jw.org/ny.

ZIMENE MUYENERA KUCHITA: Ganizirani mofatsa zimene mumakhulupirira ndiponso zifukwa zake. Fufuzani zimene Baibulo limaphunzitsa, kenako ganizirani mmene mungafotokozere ena zimene mumakhulupirirazo.

KODI N’ZOTHEKA KUCHITA ZIMENE MULUNGU AMAFUNA NGAKHALE KUTI SATANA AMATIYESA?

1 GANIZIRANI MOFATSA ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

N’chifukwa chiyani anthu ena angayankhe kuti, ayi?

N’chifukwa chiyani anthu ena angayankhe kuti, inde?

Kodi **inuyo** mumakhulupirira zotani?

Nanga n’chifukwa chiyani mumakhulupirira zimenezo?

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2 FUFUZANI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA

Yobu, yemwe anali wokhulupirika, anakwanitsa kupirira mayesero a Satana.
(Werengani mutu 12 m'buku lakuti, *Zimene Baibulo Limaphunzitsa,* ndime 6 mpaka 12.)

Werengani Yobu 1:10, 11.
Kodi Satana anachita zotani pofuna kuyesa Yobu kuti asiye kukonda Mulungu?

Werengani Yobu 1:22; 27:5.
Kodi Yobu anachita zotani pa nthawi imene Satana ankamuyesa?

Mtengo ukakhala ndi mizu yolowa kwambiri pansi, sugwa msanga kukabwera chimphepo. Mofanana ndi zimenezi, ubwenzi wathu ndi Yehova ukakhala wolimba tidzakwanitsa kupirira mayesero

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Satana amafuna kuti musiye kutumikira Mulungu, komabe Yehova angakuthandizeni kuti mupirire.

(Werengani mutu 12 m'buku lakuti, *Zimene Baibulo Limaphunzitsa,* ndime 13 mpaka 16.)

Werengani Miyambo 24:10 ndi 1 Petulo 5:8.

Kodi timadziwa bwanji kuti Satana angagwiritsire ntchito mayesero osavuta kuwazindikira (monga kuzunzidwa) komanso mayesero ovuta kuwazindikira (monga kufooketsedwa) n'cholinga choti tisiye kukhala okhulupirika kwa Mulungu?

Werengani Yobu 42:12-17 ndi Miyambo 27:11. (Onani chithunzi patsamba loyamba.)

Kodi timadziwa bwanji kuti Yehova amasangalala tikamakhalabe okhulupirika?

Kodi mumamva bwanji mukadziwa kuti zimene mungachite zingasangalatse Yehova?

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3 FOTOKOZANI ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

WINA AKANENA KUTI…

Ngati munthu akukumana ndi mavuto, ndiye kuti anachita zinazake zoipa.

MUNGANENE KUTI…

Anthu ambiri angagwirizane ndi mfundo imeneyi. Koma ine ndimakhulupirira zosiyana ndi zimenezo chifukwa…

_____

_____

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Kodi mungafotokoze zotani kuti munthuyo amvetse bwino lembalo?

_____

WINA AKANENA KUTI…

Popeza kuti Mulungu ndi wamphamvu kuposa anthufe, zimene timachita sizingamukhudze.

MUNGANENE KUTI…

N'zoona kuti Mulungu ndi wamphamvu kwambiri. Koma ndimakhulupirira kuti tikhozabe kumusangalatsa chifukwa…

_____

_____

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Kodi mungafotokoze zotani kuti munthuyo amvetse bwino lembalo?

_____

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania